Muziyamikira Zinthu Zopatulika

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwo, yerekezerani kuti nkhaniyo ikuchitika inuyo muli pomwepo. Yesani kuona m'maganizo mwanu zimene zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a m'nkhaniyi akumvera mumtima mwawo.

Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Isaki, Rabeka, Yakobo ndi Esau.

Chidule cha Nkhaniyi: Esau anagulitsa ukulu wake kwa Yakobo amene anabadwa naye mapasa.

❶ ***ONANI NKHANIYI BWINOBWINO.—WERENGANI GENESIS 25:20-34.***

Kodi Yakobo ndi Esau ankaonetsa makhalidwe otani ngakhale pamene anali m'mimba mwa mayi awo? _____

_____

_____

Kodi mukuganiza kuti Yakobo ndi Esau ankaoneka bwanji ali anyamata? _____

_____

_____

Kodi mukuganiza kuti Yakobo ndiponso Esau ankamva bwanji mumtima mwawo pamene ankakambirana zimene zili mu vesi 30 mpaka 33? _____

_____

_____

FUFUZANI MOZAMA.

Gwiritsani ntchito zinthu zofufuzira zimene muli nazo kuti mudziwe mwayi umene munthu ankakhala nawo chifukwa chokhala mwana wamwamuna woyamba kubadwa. N'chifukwa chiyani zimenezi zinali zofunika? Kodi kugulitsa mwayi umenewo ndi mbale ya mphodza kunatanthauza chiyani? _____

_____

_____

❷ ***ONANI NKHANIYI BWINOBWINO.—WERENGANI GENESIS 27:1-10, 30-38.***

Kodi mukuganiza kuti mawu a Esau ankamveka bwanji pamene ankalankhula atazindi-

kira kuti m’bale wake walandira madalitso amene mwana woyamba kubadwa ankalandira? _____

_____

_____

FUFUZANI MOZAMA.

Kodi Rabeka ndi Yakobo analakwa pokonza zoti Yakobo alandire madalitso m’malo mwa Esau? N’chifukwa chiyani mwayankha choncho? (Zokuthandizani: Werengani Genesis 25:23, 33.)

_____

_____

_____

❸ ***GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA. LEMBANI ZIMENE MWAPHUNZIRA ZOKHUDZA . . .***

Kuipa kofuna kudzisangalatsa nthawi yomweyo.

_____

_____

MMENE MUNGAGWIRITSIRE NTCHITO MFUNDOZI.

Kodi ndi zinthu zopatulika ziti zimene inuyo mwapatsidwa? _____

_____

_____

Kodi mungachite chiyani posonyeza kuti mumayamikira zinthu zopatulika? _____

_____

_____

❹ ***M’NKHANIYI, KODI NDI MFUNDO ITI IMENE YAKUKHUDZANI MTIMA KWAMBIRI, NDIPO N’CHIFUKWA CHIYANI?***

_____

_____

_____

_____

www.jw.org © 2011 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania